Zimene Mungachite Kuti Banja Lanu Lizisangalala (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* mutu 14.
Bukuli likupezekanso pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.



KODI N'CHIYANI CHIMAFUNIKA KUTI ANA AKHALE OSANGALALA?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena anganene zotani?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Ana amakhala osangalala makolo awo akamachita zinthu ngati mmene Yesu ankachitira.
(Werengani mutu 14 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 14-16.)

Werengani Maliko 10:13-16.

Kodi Yesu ankachita bwanji zinthu ndi ana ngakhale kuti ankatanganidwa?

_____

_____

_____

Werengani Luka 22:24-27 ndi Yohane 13:3-5.

N'chifukwa chiyani tinganene kuti mmene Yesu anadzudzulira ophunzira ake ndi chitsanzo chabwino kwa makolo? (Werenganinso Yeremiya 30:11.)

_____

_____

_____

Yesu ali mwana komanso atakula anasonyeza chitsanzo chabwino chomwe mabanja angatsatire

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Ana amakhala osangalala akamachita zinthu ngati mmene Yesu ankachitira.

(Werengani mutu 14 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 17-19.)

Werengani Luka 2:51, 52; 22:42.

Kodi achinyamata angaphunzire chiyani kwa Yesu pa nkhani ya kukhala womvera? (Werenganinso Aefeso 6:1-3.)

Werengani Mateyu 4:1-10.

Kodi Yesu anasonyeza bwanji chitsanzo chabwino pokana kugonja atakumana ndi mayesero?

N'chiyani chimakusangalatsani kwambiri mukaganizira zimene Yesu anachita?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA WANENA KUTI…

Baibulo limakhwimitsa zinthu pa nkhani yopereka chilango.

MUNGAYANKHE KUTI…

N'zoona kuti Baibulo limalimbikitsa makolo kupereka chilango kwa ana awo. Koma sindikukhulupirira kuti limalimbikitsa makolo kuti azikhwimitsa zinthu chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti?

_____

Poganizira zimene munthuyo wakuuzani, kodi mungagwiritse ntchito bwanji mfundo ya palembali kuti mumuthandize?

_____

NGATI WINA WANENA KUTI…

Nkhani ya kukhala womvera imapondereza achinyamata. Achinyamata aziloledwa kuchita chilichonse chomwe akufuna.

MUNGAYANKHE KUTI…

Anthu ambiri angaterodi. Koma ine ndikukhulupirira kuti…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti?

_____

Poganizira zimene munthuyo wakuuzani, kodi mungagwiritse ntchito bwanji mfundo ya palembali kuti mumuthandize?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania